# KABUKU KA MAYESO

## UTHENGA WABWINO WA MARKO

### GAWO 1

NAWA MALANGIZO OYENERA KUTSATIRA POLEMBA MAYESO

1. Lembani dzina lanu mooneka bwino pamalo pamene mwapatsidwa. Lembani nambala yanu imene mwapatsidwa. Ndipo onetsetsani kuti nthawi zonse muyenera kumagwiritsa ntchito dzina lomweli osasinthasintha.
2. Mayankho a funso lililonse akhoza kupezeka mu phunziro limene mukuchita kapena pa ndime zimene zapelekedwa kuti muwerenge m'Buku Lopatulika. Motero mukhoza inu kuwerenga phunziro lanulo kapena Buku Lopatulika kuti mupeze mayankho a mafunsowo.
3. Mudzapeza kuti pa funso lililonse pali mayankho atatu. Koma yankho loona kwenikweni ndi limodzi. Motero yankho lokhozalo liri ndi nambala ndipo muyenera kulemba nambala yake ya yankho lokhoza lija pa mzere umene mwapatsidwa pambali pake pafunsolo. Phunzirani kuchokera pa chitsanzo chimene taikachi ndipo musayambe kuyankha mafunso ena mpaka mutazindikira bwino zoyenera kuchita pofuna kuyankha funso.

---

CHITSANZO:

________ 1. Amayi ake a Yesu anali (1) Sara, (2) Mariya, (3) Elizabeti. Tikudziwa bwino lomwe kuti yankho lokhoza ndi Mariya, ndipo ndi nambala (2). Motero lembani nambala 2 pa mzere umene uli kumbali pa funso.

Nambala iyenera kulembedwa pamwamba pa mzere wapatsidwao koma musalembe pansi kapena mkati mwa mzerewo ayi. Kapenanso musalembe mzere pansi pa yankho lokhozalo ayi. Choyenera kuchita ndikulemba NAMBALA YOKHAYO PA MWAMBA PA MZERA UMENE MWAPATSIDWA PAMBALI PA FUNSO.

---

4. Pamene mukuchita mayesowa, chonde muyenera kusamala zedi. Werengani funso mosamala, ndipo muliganizire bwino chimene chikufunika. Ndipo musapupulume poyankha koma dekhani mtima kuti muyankhe zokhoza ndikuchita bwino. Musalembe yankho mongoyerekezera kapena limene simukulikhulupirira kuti ndi lokhoza. Werenganinso Buku Lopatulika kapena phunziro lanu kufuna kutsimikiza ngati yankho lanu ndilokhozadi.
5. Mukhoza kukhala pamodzi ndi mzanu kapena pagulu kumaphunzira maphunziro nonse pamodzi. Mukhoza kumakambirana za phunziro limene mukuchita ngakhalenso mayeso

anu. Chinthu chachikuru choyenera kumachikumbukira ndi chakuti iwuyo muyenera kulemba mayeso ainu nokha. Chonde musakopere mayankho kuchokera kwa mnzanu ayi. Mukhoza kuyang'anira m'buku lanu la maphunziro kapena kudziwerengera nokha Buku Lopatulika, koma chonde musakopere mayankho kuchokera pa mayeso amunthu wina.

6. CHOFUNIKIRA KWAMBIRI: Muyenera kuchita zotsatirazi mayeso anu asanatumizidwe kukachonga:
   a) Muyenera kuwerenga ndime zonse zimene mwapatsidwa pa phunziro lililonse.
   b) Muyenera kuti muloweze ndime zonse za pamtima zimene mwapatsidwa kuti muloweze.

7. CHOFUNIKIRA CHINA: Pamene mwamaliza kuyankha mafunso onse amene ali mu kabuku ka mayeso muyenera kukapinda kabukuka bwino ndikukamatira mu enivelopu. Ndipo mutitumizire ife kuno pogwiritsa ntchito adiresi ya BIBLE WAY CORRESPONDENCE SCHOOL.

8. CHOFUNIKIRA: Muyenera kutsimikiza kuti sitampa imene mwamata pa enivelopu ndi yokwanira. A Bible Way Correspondence School sadzalandira maenivelope amene adzafunika kuwomboledwa kuno. A Bible Way Correspondence School sawombola enivelopu iliyonse imene ilibe sitampa yokwanira.

Mukamaliza maphunziro onse khumi ndi awiri ndipo mukakhoza mudzalandira chikalata chachitsimikizo (satifiketi) yokongola kwambiri yomwe mukhoza kuyika muja mumakhala zithunzi zina monga pikicha felemu. Ndipo satifiketi imeneyi ndi mphotho imene imapatsidwa kwa iye amene wamaliza bwino maphunziro ake. Koma siyoyenera kuti mukhoza kukafunsira ntchito ayi.

Chinthu chofunikira kwambiri kuti muziphunzira maphunzirowa ndi mtima wakupemphera. Pemphani Mulungu kuti akuthandizeni kuzindikira zoonadi zodabwitsa ziri m'Buku Lopatulika pamene mukuphunzira mawu ake. Ndipo Mulungu mwini adzakutsogolerani kuti mudziwe chipulumutso chiri mwa Yesu Kristu. Ngati muli mkristu kale tipemphera kuti maphunzirowa adzakuthandizani kuti mukhale wamphamvu mchikhulupiriro chachikristu.



NDAMANGA PA MAPHUNZIRO ONSEWA:

Ngati mulikufuna kuthirira ndamanga pa maphunzirowa monga zimene zakuthandizani pa maphunzirowa, mukhoza kutilembera pa pepalali. (Muyenera kudziwa kuti zimene mulembe pepalazo sizili mbali ya mayeso anu motero sizichongedwa ayi.)

## KUPEMPHA MAPHUNZIRO ENA

Tsopano pakuti mwamaliza maphunziro a Gawo 1, tiri ndichiyembekezo chakuti mudzafuna kutipitiriza kumaphunzira Mawu a Mulungu kupyolera mu Bible Way Correspondence School. Kuno tili ndi maphunziro enanso amene mukhoza kuchitanso. Chimene mungachite ndikulemba zonse zofunikira pa chikalatachi ndipo muyenera kutumiza ndalama zokwanira maphunziro amene mukufuna. Ngati mutumiza chikalatachi choitanitsira maphunziro ena pamodzi ndi mayeso anu, mudzalandira maphunziro anu atsopanowo pamodzi ndi satifiketi ya mayeso amene mwachita kale. Musachedwe, tumizani mwamsanga lero lino!

Inde, ndikufuna kupitiriza kuphunzira Mawu a Mulungu kupyolera mu Bible Way Correspondence School, chonde nditumizireni maphunziro amene ndasankha pansipa. Ndipo ndatumiza ndalama zokwana K__________ za maphunziro amene ndasankhawa.

DZINA LANU______________________________Nambala yanu______________

Adiresi yanu________________________________________________________

Sankhani maphunziro amene mukufuna kuchita:
- Uthenga Wabwino wa Marko, Gawo 2
- Chikonzero Chodabwitsa Cha Mulungu
- Kukula Monga Akristu
- Malongosoledwe a Buku Lopatulika

## MAYESO A PHUNZIRO 11

___10. Ngati tingawaone anthu m'njira yoyenera, tikhoza kuwaona iwo monga (1) Yesu anali kuwaona iwo, (2) afalisi anali kuwaona, (3) mitengo.

## MAYESO A PHUNZIRO 12

Kubvomereza:

Ndaphunzira kuloweza mawu apamtima Marko 8:36 ndipo ndawabwereza kuuza mnzanga. (Lembani dzina lanu.)________

Ndawerenga ndime zonse zimene zinalembedwa pa phunziro 12. (Lembani dzina lanu.)____________________

___1. Yesu anawafunsa ophunzira ake kuti Iye ali yani chifukwa Yesu anafuna kudziwa (1) ngati iwo anali kuzindikira kuti Iye anali ndani , (2) ngati iwo anali kudziwa dzina lake, (3) ngati iwo anali kudziwa zimene anthu ena anali kumanena.

___2. Amene anayankha funso la Yesu pamene Iye anafunsa kuti ali yani ndi (1) Yohane, (2) Petro, (3) Yakobo.

___3. Petro ananena kuti Yesu anali (1) munthu wabwino, (2) Mpulumutsi, (3) mphunzitsi wamkuru.

___4. Ayuda anali kuganizira kuti Mpulumutsi (1) sadzabwera, (2) adzazunzika ndi kufa, (3) adzakhazikitsa Israyeli monga ufumu wamphamvu.

___5. Pamene Yesu ananena kuti pa thanthwe limene ndidzamangapo mpingo wanga, anali kutanthauza (1) Petro adzakhala mutu wa mpingo, (2) Iye Yesu anaika nyumba pa thanthwe lina lake, (3) Iye adzamanga mpingo wake pa maziko achibvomerezo chakuti Iye ndiye Kristu.

___6. Yesu anawauza ophunzira mu Marko 8:31 kuti Iye (1) adzazunzika kwambiri, (2) adzayesedwa, (3) adzazemba imfa.

___7. Yesu ananena kuti iwo amene adzamutsatira Iye ayenera kukhala okonzeka (1) kukhala okha, (2) kudzikana okha, (3) azisala kudya kawirikawiri.

___8. Yesu ananena kuti iye amene apulumutsa moyo wake (1) adzausunga, (2) adzasangalala, (3) adzautaya.

___9. Yesu ananena kuti palibe chimene munthu angaphindule ngati angalandire dziko lonse lapansi koma nkutaya (1) moyo wake, (2) kutchuka kwake, (3) chuma chake chonse.

___10. Ngati ife tikuchita naye manyazi Yesu pamaso pa anthu, Iyenso (1) adzachita nafe manyazi pamaso pa Atate wakukwamba, (2) adzatitengabe kupita naye kumwamba pakuti palibe china angatichite, (3) adzakondwera nafe.



## UTHENGA WABWINO WA MARKO, GAWO 1

DZINA____________________ Nambala yanu 026657D

Adiresi yanu____________________

## MAYESO A PHUNZIRO 1

Kubvomereza:

Ndaphunzira kuloweza mawu apamtima Yohane 20:31 ndipo ndanena mnzanga akumvera. (Lembani dzina lanu.)________

Ndawerenga ndime zonse zimene zinalembedwa pa phunziro 1. (Lembani dzina lanu.)____________________

___1. Mawu apamtima, Yohane 20:31 akutiphunzitsa kuti Buku Lopatulika linalembedwa (1) kotero kuti ife tikhulupirire kuti Yesu ndi Mwana wa Mulungu, (2) kotero kuti tikhoza kuona kusiyana pakati pa chikristu ndi zipembedzo zina, (3) kotero kuti wolemba mabuku a Buku Lopatulika adzionetsere okha kuchenjera kwao.

___2. Pa ndime yoyamba, Marko akunena kuti Yesu anali (1) Mneneri, (2) Mphunzitsi, (3) Mwana wa Mulungu.

___3. Mawu akuti "Uthenga Wabwino" amatanthauza (1) Mbiri yabwino, (2) Mbiri yoipa, (3) kulalikira.

___4. Uthenga Wabwino umene Marko analemba unali wa (1) Yohane akusonyeza anthu kufunikira kwa kumadya dzombe ndi uchi, (2) kukhala ku chipululu kunali kwabwino kuposa ku Yerusalemu, (3) Mulungu anatuma Mwana wake Yesu Kristu padziko lapansi.

___5. Ntchito yaikuru ya Yohane m'Batizi inali (1) kukhala m'chipululu, (2) kukonza njira ya Yesu Kristu, (3) kudya dzombe ndi uchi mthengo.

___6. Yohane anali kubatiza iwo amene anabwera (1) kudzafuna kulowa mpingo, (2) akulapa machimo awo, (3) kudzafuna kudziwa kuti Yohaneyo anali yani.

___7. Kutembenuka mtima kwenikweni kumatanthauza (1) kumva chisoni pakuti machimo amakupangitsa kuti uzunzike, (2) kumapita ku chalichi, (3) kumva chisoni pa zoipa zimene wachita ndipo kuzisiya ndi kusintha.

___8. Paulo mu Aroma 6:4 akunenamo kuti ubatizo ndi chithunzi (1) chakuti madzi atsuka machimo athu, (2) chakuti mpingo ukhoza kukhululukira machimo, (3) chakuti taikidwa m'manda ndi Kristu ndikuuka kwa akufa kulowa m'moyo watsopano.

___9. Yohane m'Batizi ananena kuti Yesu adzapatsa omutsatira (1) chuma chambiri, (2) moyo wopanda mabvuto, (3) Mzimu Woyera.

___10. Yohane m'Batizi anaphunzitsa kuti Yesu (1) ali wofanana ndi Yohane, (2) wamkulu woposa Yohane, (3) wochepa koposa Yohane.

## MAYESO A PHUNZIRO 2

Kubvomereza:
Ndaphunzira kuloweza mawu apamtima, Marko 1:15 ndipo ndalibwereza kuuza mnzanga. (Lembani dzina lanu.)________
Ndawerenga ndime zonse zimene zinalembedwa pa phunziro 2. (Lembani dzina lanu.)________________________

___1. Yesu anayamba utumiki wake wapoyera (1) pakuukitsa munthu wakufa, (2) pobatizidwa, (3) poyesedwa.

___2. Yesu anasonyeza kuti Iye anatsimikiza chiphunzitso cha Yohane (1) powauza anthu ena kuti apite kwa Yohane, (2) pomakhala kutali ndi Yohane, (3) polandira ubatizo wa Yohane.

___3. Malinga ndi Mateyu 3:15, Yesu ananena kuti ayenera kubatizidwa kukwaniritsa (1) ulosi, (2) chilungamo chonse, (3) utumiki wa Yohane.

___4. Mawu amene anachokera kumwamba pa kubatizidwa kwa Yesu anati (1) Uyu ndiye mwana wanga wokondedwa, (2) Pita kumbuyo kwanga, (3) Muka usakachimwenso.

___5. Yesu anayesedwa amene anamuyesa Yesu ndi (1) Mzimu wa Mulungu, (2) Yudasi, (3) Satana.

___6. Yesu anayesedwa kwa masiku (1) khumi, (2) makumi anayi, (3) makumi awiri.

___7. Yesu anayesedwa chifukwa chakuti (1) Iye anali woipa, (2) Mulungu anamkwiyira Yesu, (3) Satana anafuna kuwononga Woyera wa Mulunguyu.

___8. Malinga ndi Marko 1:14, Yesu anayamba kulalikira ku (1) Yudeya, (2) Yerusalemu, (3) Galileya.

___9. Yesu anali kulalikira kuti (1) anthu wochimwa ayenera kulapa ndikukhulupirira Uthenga, (2) ubatizo udzatipulumutsa, (3) anthu ayenera kutsatira Yohane m'Batizi.

___10. Yesu anasankha ophunzira ake kuti (1) akhoza kuwaphunzitsa kuti atumikire Mulungu, (2) azikhala ndi gulu la anthu ocheza nawo, (3) awapatse ntchito yamalipiro ochuluka.



## UTHENGA WABWINO WA MARKO, GAWO 1

DZINA________________________Nambala yanu__________

Adiresi yanu________________________________

### MAYESO A PHUNZIRO 11

Kubvomereza:
Ndaphunzira kuloweza mawu apamtima Marko 7:37 ndipo ndawabwereza kuuza mnzanga. (Lembani dzina lanu.)________
Ndawerenga ndime zonse zimene zinalembedwa pa phunziro 11. (Lembani dzina lanu.)________________________

___1. Kuchiritsidwa kwa mwana wa mkazi wa mzimayi uja waku Suro-Fonika kukosonyeza kuti (1) Yesu anali kukonda anthu ena koposa ena, (2) kunalibe ayuda amene akadakhoza kuwachiritsa, (3) Yesu anakonda anthu onse.

___2. Yesu anachiritsa mwana wa mkazi wa mzimayi waku Suro-Fonika kuja (1) pomukhuza, (2) pomudzodza mafuta amtengo wapatali, (3) polankhula chabe mawu akuchiritsa.

___3. Njira imene Yesu anachiritsira munthu wogontha mkutu ndi wosalankhula ija kusonyeza kuti (1) Iye anali wokhuzidwa ndi zosowa za munthu aliyense, (2) Iye anali kufuna kumasokoneza afalisi, (3) sakadatha kuchitira mwina.

___4. Ndemanga zimene anthu analankhula pamene Yesu anachiritsa munthu wosamva ndi wosalankhula (1) anachitiranji Iye zimenezi, (2) Iye anachita zinthu zonse bwino zedi, (3) sanali woyenera kuchita zimenezo.

___5. Tsopano pamene Yesu ananena kuti akufuna kuwadyetsa makamu aja, ophunzira ake (1) anakumbukira za nthawi yoyamba ija ndipo anadziwa kuti Iye akhoza kuwadyetsadi, (2) ayamba kufunafuna mnyamata amene anali ndi chakudya, (3) anaganiza kuti ndikosatheka.

___6. Kudyetsa chikhamu cha zikwi zisanu ndiponso kudyetsa chikhamu cha zikwi zinayi zinali (1) nthano ziwiri zimene Yesu analankhula kwa anthu koma sizinachitike, (2) nkhani imodzi koma yonenedwa mnjira ziwiri zosiyana, (3) zodabwitsa ziwiri zimene zinachitika malo osiyana ndi nthawi zosiyana koma zinali ndi tanthauzo lofanana.

___7. Yesu anakana kuwapatsa afalisi chizindikiro pakuti iwo (1) sanali ophunzira ake, (2) sanali kufunafuna choonadi ndi mtima wonse, (3) anali wochokera ku Yerusalemu.

___8. Yesu anawadzudzula ophunzira ake (1) pokhala wochedwa kuphunzira, (2) pokhala wochedwa kulankhula, (3) pakuchedwa kupalasa bwato.

___9. Kuchiritsidwa kwa wakhungu waku Betesaida kunali kwachilendo pakuti (1) Yesu anamkwapula munthu wakhungu uja, (2) Yesu anamkalipira iye, (3) Yesu anamuchiritsa iye pang'onopang'ono.

## MAYESO A PHUNZIRO 10

Kubvomereza:
Ndaphunzira kuloweza mawu apamtima Marko 7:15 ndipo ndawabwereza kuuza mnzanga. (Lembani dzina lanu.)________
Ndawerenga ndime zonse zimene zinalembedwa pa phunziro 10. (Lembani dzina lanu.)__________

___1. Gulu la alembi ndi afalisi anafika kwa Yesu kuchokera ku (1) Betelehemu, (2) Yerusalemu, (3) Nazarete.

___2. Alembi ndi afalisi aja anafika (1) kudzampeza chifukwa Yesu, (2) kudzaphunzira nawo zimene Yesu anali kuphunzitsa, (3) kudzafuna chithandizo kuchokera kwa Iye.

___3. Alembi ndi afalisi anadzudzula ophunzira a Yesu kuti (1) chifukwa chakuti sanali kudya chakudya, (2) sanali kumasamba m'manja mwawo moyenera, (3) sanali kusamba m'manja mwao molingana ndi miyambo ya makolo awo.

___4. Yesu anawayankha alembi ndi afalisi kuti (1) anthu ayenera kumvera malamulo a Mulungu koposa miyambo ya anthu, (2) ayenera kubwerera ku Yerusalemu, (3) sayenera kusamba m'manja mwao.

___5. Mawu akuti "chiphamaso" amatanthauza (1) munthu wonyenga anthu pomasonyeza ngati akuchita zimene akunena, (2) sing'anga, (3) wansembe.

___6. Yesu ananena kuti pamene akutsatira malamulo awo onse alembi aja ndi afalisi anali (1) kukondweretsa Mulungu, (2) kupereka chitsanzo chabwino kwa anthu, (3) kusiya malamulo a Mulungu.

___7. Chipembedzo chenicheni chimachokera (1) kumakhalidwe abwino, (2) kumaphunziro abwino ndi apamwamba, (3) Mulungu.

___8. Kwa otsatira a Yesu chipembedzo ndi (1) kumadzionetsera kunja kokha kuti ukusunga malamulo ndi miyambo, (2) ukakhala membala wampingo, (3) chisomo cha Mulungu chochitika mumtima mwa munthu.

___9. Yesu ananena kuti kudetsedwa ndi pamene munthu (1) sakutsatira miyambo yamakolo, (2) ali ndi mtima wodetsedwa pamaso pa Mulungu, (3) ali wosabatizidwa.

___10. Ulamuliro wachipembedzo cha chikristu umachokera kwa (1) wansembe, (2) Buku Lopatulika, (3) m'maganizo athu.



## UTHENGA WABWINO WA MARKO, GAWO 1

DZINA__________________________Nambala yanu__________

Adiresi yanu__________________________________

### MAYESO A PHUNZIRO 3

Kubvomereza:
Ndaphunzira kuloweza mawu apamtima, Marko 2:10 ndipo ndabwereza kuuza mnzanga. (Lembani dzina lanu.)________
Ndawerenga ndime zonse zimene zinalembedwa pa phunziro 3. (Lembani dzina lanu.)__________

___1. Yesu anali kuphunzitsa monga (1) alembi ndi afalisi, (2) munthu wokaika, (3) munthu mwini mphamvu.

___2. Ulamuliro wa Yesu pakulalikira unasonyezedwa (1) pakumapita Iye ku masunagoge, (2) pochiritsa munthu wa mzimu wonyansa, (3) pakulankhula kwa ophunzira ake.

___3. Yesu anali kuchiritsa chifukwa chakuti (1) Iye anakonda anthu, (2) Iye anafuna kuti anthu azimulipira anafuna kupezamo cholowa pomulipira anthu, (3) Iye anafuna kuyamikiridwa ndi anthu.

___4. Pamene Yesu anachiritsa apongozi ake a Petro, mayiyo (1) anangogonabe kufuna kupuma, (2) anapita kukagula zinthu, (3) anayamba kuwatumikira.

___5. Wodwala anafika nawo kwa Yesu dzuwa litalowa chifukwa (1) anthu adakatha kuyenda bwino pamene kukuzizirira madzulo, (2) tsiku la sabata linali litatha, (3) anthu sakadatha kuzindikiridwa.

___6. M'mamawa kwambiri Yesu (1) anapita kwa yekha kukapemphera, (2) sanadzuke msanga, (3) anayambanso kulalikira.

___7. Munthu wakhate uja sanali kutsimikiza kuti Yesu (1) ali ndi mphamvu zotha kumuchiritsa, (2) akhoza kudzipereka kumuchiritsa, (3) akhoza kukhala ndi nthawi yomuchiritsa.

___8. Pomuchiritsa munthu wakhate uja Yesu anali kutsimikiza kuti (1) munthuyo sanali kudwala kwambiri, (2) khate sirinali lobvuta kwambiri monga anthu ankaganizira, (3) Yesu anali ndi mphamvu za umulungu monga Mulungu mwa thupi lamunthu.

___9. Munthu wodwala amene sanali kutha kuyenda anabweretsedwa kwa Yesu ndi (1) abwenzi awiri, (2) abwenzi anayi, (3) abwenzi asanu ndi m'modzi.

___10. Yesu anasonyeza kuti ali ndi mphamvu yokhululukira machimo (1) powauza anthu kuti Iye ali nazo mphamvu, (2) pomusiya wodwalayo yekha, (3) pochiritsa wodwalayo.

## MAYESO A PHUNZIRO 4

Kubvomereza:

Ndaphunzira kulowe mawu apamtima, Marko 2:27 ndipo ndabwereza kunena kwa mnzanga. (Lembani dzina lanu.) ________

Ndawerenga ndime zonse zimene zinalembedwa pa phunziro 4. (Lembani dzina lanu.) ________________

___1. Utumiki wa Yesu unali wosiyana ndi wa ena onse pakuti Iye anali kuphunzitsa kuti anthu ayenera kukhala (1) pachiyanjano chabwino ndi Mulungu mumtima mwawo, (2) molingana ndi miyambo ya makolo, (3) ndi ufulu wakuchita chilichonse akufuna.

___2. Ulamuliro wonse wonena za chikhulupiriro ukuchokera (1) mu maganizo kapena mitima yathu, (2) mumpingo, (3) M'Buku Lopatulika.

___3. Ulamuliro wa Yesu unali wosiyana ndi wa ena pakuti ulamuliro wake unali kuchokera (1) kwa aphunzitsi ena, (2) kwa Mulungu, (3) M'Chipangano Chakale.

___4. Pamene Mateyu anamukonzera Yesu phwando ndi kuitana amisonkho anzake, Yesu (1) anakana kukakhala nawo pa phwandolo pakuti amisonkho anali wochimwa zedi, (2) anapita koma anakhala pa gome la yekha kusiyana ndi amisonkho, (3) anapita ndikukadya pamodzi ndi amisonkho.

___5. Afalisi anali kusala chakudya (1) kuti ayamikiridwe, (2) kuti alemekeze Mulungu, (3) kuti adzionda pakuti anali anthu wonenepa zedi.

___6. Yesu ananena nthano za matumba a zikopa za mvinyo ndi chigamba chatsopano chosokedwa pa chobvala chake kufuna kusonyeza kuti (1) ulimi masiku aja unali wosiyana, (2) kusoka zobvala masiku aja kunali kosiyana, (3) utumiki wake unali wosiyana ndi wa ena.

___7. Yesu ananena kuti (1) munthu analengedwa kuti azisunga tsiku la sabata, (2) Iye anali Ambuye wa Tsiku la sabata, (3) Iye sangathe kusintha tsiku la sabata.

___8. Kuchokera pa Machitidwe 20:7 ndi 1 Akorinto 16:2 taphunzirapo kuti akristu am'Chipangano Chatsopano anali kulambira pa (1) tsiku loyamba la sabata (2) lolemba, (3) loweruka.

___9. Malingana ndi mawu apamtima, Marko 2:27 (1) kukadakhala bwino tsiku la sabata likadasiyidwa kupangidwa, (2) munthu analengedwa chifukwa cha tsiku la sabata, (3) tsiku la sabata linalengedwa chifukwa cha munthu.

___10. Pamene Yesu anachiritsa munthu wodwala pa tsiku la sabata kunasonyeza kuti (1) Yesu sakadatha kuchiritsa munthu pa tsiku lina, (2) Iye anafuna kuwabvutitsa afalisi, (3) Iye anaganizira kuti kuchiritsa munthu wodwala kunali kofunikira koposa kusunga mwambo wakalekale.



## UTHENGA WABWINO WA MARKO, GAWO 1

DZINA________________________Nambala yanu________

Adiresi yanu________________________________

### MAYESO A PHUNZIRO 9

Kubvomereza:

Ndaphunzira kuloweza mawu apamtima Marko 6:50 ndipo ndawabwereza kuuza mnzanga. (Lembani dzina lanu.)________

Ndawerenga ndime zonse zimene zinalembedwa pa phunziro 9. (Lembani dzina lanu.)________________

___1. Ophunzira anayang'ana chikhamu cha anthu chija. Ndipo anazindikira kuti alibe chakudya chokwanira ndipo (1) anaganiza kuti palibe chimene angachite, (2) anafuna kuwadyetsa, (3) anawatuma kukagula china.

___2. Yesu anadyetsa chikhamu cha anthu chija ndi (1) madengu khumi ndi awiri achakudya, (2) ufa wodzadza thumba lalikuru limodzi, (3) chakudya chochepa chokwanira mwana m'modzi cha masana chomwe chinali mikate isanu ndi tinsomba tiwiri.

___3. Yesu anadyetsa chikhamu cha anthu (1) mazana asanu, (2) zikwi ziwiri, (3) zikwi zisanu.

___4. Kudyetsa makamu aja kumatiphunzitsa ife kuti (1)pamene tikupereka zimene tiri nazo kwa Mulungu Iye amazigwiritsa ntchito kudalitsa anthu ambiri, (2) anthu sasowa zinthu, (3) tizidya nsomba nthawi zambiri.

___5. Yesu atawauza anthu kuti azipita Iye (1) anakwera kuphiri kukapemphera, (2) anapita mumzinda kukagula chakudya, (3) anapita ku gombe mphepete mwa nyanja ndikukapeza bwato.

___6. Pamene Yesu anafika kwa ophunzira ake panyanja paja, Iye anali (1) m'bwato, (2) kusambira mnyanja, (3) kuyenda pa nyanja.

___7. Pamene Yesu anafika pa bwato lija panthawi imene mphepo inali kuomba (1) namondwe anapitirira koposa, (2) nyanja inakhala bata, (3) ophunzira nkuti ali mtulo.

___8. Mawu apamtima Marko 6:50 akutiphunzitsa ife (1) palibe amene amatisamalira ngati tikuchita mantha kapena ayi, (2) tiyenera kuyang'ana kwa Yesu pamene tikuchita mantha, (3) tisamakwera bwato panyanja.

___9. Pamene iwo anafika ku Genesalete (1) ophunzira aja anali okha pamodzi ndi Yesu basi, (2) anthu sanali kufika kwa Yesu, (3) makamu ambiri a anthu anasonkhana.

___10. Panthawi ya mazunzo Yesu anawafunsa ophunzira ake (1) kuti kodi ena onse ali kuti, (2) kodi nanunso mukufuna kuchoka, (3) chikuchitika nchiyani kwa Ine.

## MAYESO A PHUNZIRO 7

___10. Mphamvu za Yesu ndizokwanira kugonjetsa (1) zobvuta zina koma sizonse, (2) zobvuta zonse pa moyo wamunthu, (3) palibe chobvuta chimene tikukumana nacho muno mu Afrika masiku ano angathe.

## MAYESO A PHUNZIRO 8

Kubvomereza:

Ndaphunzira kuloweza mawu apamtima Marko 6:4 ndipo ndabwereza kumuuza mnzanga. (Lembani dzina lanu.)__________

Ndawerenga ndime zonse zimene zinalembedwa pa phunziro 8. (Lembani dzina lanu.)__________

___1. Chimodzi mwa zinthu zimene zinalikubvutitsa mitima ya anthu aku Nazarete chinali chakuti Yesu nthawi zonse anali (1) mphunzitsi, (2) m'misiliwogwira ntchito, (3) mlendo.

___2. Yesu sanathe kuchitanso zodabwitsa zazikuru zina ku Nazarete chifukwa cha (1) kusakhulupirira kwa anthu, (2) kusauka kwa anthu, (3) chimwemwe cha anthu.

___3. Ophunzira anatumidwa (1) kukasonkhanitsa ndalama, (2) kukalalikira ndi kukachiritsa, (3) kukaso koneza alembi ndi afalisi.

___4. Ophunzira aja sanatenge zinthu zina zambiri zoyenera paulendo. Ichi chinali kusonyeza (1) kudzipereka kwao kulandira ndi kulandiridwa ndi anthu onse, (2) kulephera kukonzekera ulendo, (3) umphawi.

___5. Yesu anali kugwiritsa ntchito njira zochiritsira zakale ndipo (1) sanali kuonjezera kanthu, (2) anali kuwonjezera mankhwala ena amizu imene anakatenga kwa sing'anga wina, (3) anali kuwonjezerapo mphamvu ya Iye mwini.

___6. Herode anaganiza kuti Yesu anali (1) Yohane m'Batizi kuti wauka kwa akufa, (2) Eliya, (3) mneneri wina wam'Chipangano Chakale.

___7. Yohane m'Batizi anaphedwa (1) moponyedwa miyala, (2) modulidwa mutu, (3) mochita kupachikidwa.

___8. Herode analamula kuti Yohane aphedwe chifukwa (1) iye anali kuganizira kuti Yohane anali munthu woipa, (2) iye analonjeza mopusa kwa mwana wamkazi wa Herodiya, (3) Yohane anali atakalamba ndipo anali kumadwaladwala motero Herode anaganiza zomutsiriza kuti apumule kuzosautsa zake.

___9. Pamene ophunzira a Yesu anabwerera kwa Iye, anamuuza (1) za zimene iwo anali kupatsidwa, (2) zimene iwo anachita, (3) zimene iwo anasowa.

___10. Yesu anawauza ophunzira aja (1) kuti abwerere ndikukalalikiranso, (2) kuti akawuze aliyense zimene iwo anachita, (3) achoke limodzi ndi Iye apite kumalo awokha kukapumula.



# UTHENGA WABWINO WA MARKO, GAWO 1

DZINA__________________________Nambala yanu__________

Adiresi yanu__________________________________

## MAYESO A PHUNZIRO 5

Kubvomereza:

Ndaphunzira kuloweza mawu apamtima Marko 3:25 ndipo ndabwereza kwa mnzanga kumuuza. (Lembani dzina lanu)__________

Ndawerenga ndime zonse zimene zinalembedwa pa phunziro 5. (Lembani dzina lanu)__________

___1. Yesu anasiya kumaphunzitsa mumasunagoge chifukwa (1) Iye anali kuchita mantha ndi anthu, (2) Iye anali kuchita mantha ndi alembi ndi afalisi, (3) Iye anafuna kulalikira ndi kuphunzitsa wopanda wina womubvutitsa.

___2. Yesu sanafune kuti mizimu yoipa ija ilankhule za Iye chifukwa (1) mizimuyo siinali kunena zoona, (2) chifukwa maziko a umboni wawo anali odetsedwa kale, (3) anthu sakadatha kuzimvera.

___3. Yesu anasankha ophunzira khumi ndi awiri chifukwa (1) Yesu sanali kukonda anthu enanso, (2) Iye anafuna kuwaphunzitsa bwino kwambiri, (3) Iye anafuna kusiya kumalalikira.

___4. Mulungu amapatsa anthu ake mphamvu zakuchiritsa, kulalikira, kuturutsa ziwanda (1) kuti zitengere ulemereo ndi ulemu Iye mwini, (2) kuti anthu akhale ali wotanganidwa, (3) kuti zilemekeze anthu ena.

___5. Abwenzi ena anamudzudzula Yesu kuti ndi (1) wankhaza, (2) wamisala, (3) ndi munthu wansangala nthawi zonse.

___6. Alembi anamudzudzula Yesu (1) kuti amayanjana ndi belezebulo, (2) pakuti anali mneneri, (3) pakukhala munthu wofatsa ndi wokonda mtendere.

___7. Machitidwe 4:12 akutiphunzitsa ife kuti (1) tikhoza kupulumutsidwa kudzera mchipembedzo chilichonse, (2) palibe chifukwa chokwanira kuti tifune kupulumutsidwa, (3) palibe chipulumutso koma mwa Yesu yekha.

___8. Tchimo losakhululukidwa ndi (1) kusakhulupirira komwe kuli kukana Kristu monga Ambuye ndi Mpulumutsi, (2) kupha munthu, (3) chigololo.

___9. Yesu ananena kuti banja lake lenileni ndi (1) Mariya ndi ana ake, (2) iwo amene akuchita chifuniro cha Mulungu, (3) ayuda onse.

___10. Kuti tikalowe ufumu wa Mulungu tiyenera (1) kubadwa kwatsopano, (2) kubatizidwa, (3) tikhala membala wa pfuko lina.

## MAYESO A PHUNZIRO 6

Kubvomereza:

Ndaphunzira kuloweza mawu apamtima Marko 4:20 ndipo ndawabwereza kuuza mnzanga. (Lembani dzina lanu.)________

Ndawerenga ndime zonse zimene zinalembedwa pa phunziro 6. (Lembani dzina lanu.)________

___1. Fanizo ndi (1) munthu wofesa mbewu, (2) m'Samariya, (3) nthano imene ikunenedwa mofanizira chinthu pofuna kuphunzitsa choonadi.

___2. Fanizo limamasulira (1) palibe chinthu chimodzi chomwe (2) choonadi chimodzi kapena zoonadi ziwiri, (3) kalikonse kamene ife tikufuna kuchita.

___3. Pofuna kuzindikira fanizo tiyenera (1) kuwonjezera matanthauzo athu, (2) kupeza kumasulira kwina kwake, (3) kupeza choonadi chimene chinali cholinga cha wolankhulayo.

___4. Mu fanizo la wofesa mbewu nthaka zosiyanasiyana, mbewu ikuyimirira (1) Mawu a Mulungu, (2) munthu womvetsera mawu, (3) palibe choimirira.

___5. Mu fanizo la wofesa mbewu, wofesayo (1) akubisa mbewu, (2) akugwa pa nthaka ya minga, (3) akufalitsa Uthenga Wabwino.

___6. Fanizo la wofesa mbewu likutiphunzitsa ife kuti (1) alimi ena si alimi abwino, (2) mbewu zina simbewu zabwino, (3) anthu osiyanasiyana amaulandira uthenga mosiyananso.

___7. Nthaka yolimba m'mbali mwanjira ikuyimirira anthu amene (1) salandira bwino mawu a Mulungu amene akuwamvera, (2) sakonda Buku Lopatulika, (3) salandira bwino mawu a Mulungu pamene atamva.

___8. Nthaka ya tanthwe ikuyimirira anthu amene (1) akumva mawu a Mulungu koma sapitirira kutsatira Mulungu, (2) akukana kumvera, (3) sakonda Buku Lopatulika.

___9. Fanizo la nyali likusonyeza kuti (1) nyali sizimapereka kuwala kwabwino, (2) mkristu ayenera kumachitira umboni za chisomo cha Mulungu, (3) palibe phindu kumalalikira Mawu a Mulungu.

___10. Fanizo la kambewu ka mpiru limasonyeza kuti (1) anthu ali ngati kambewu kampiru, (2) ufumu wa Mulungu udzakula, (3) kambewu kampiru ndi kakang'ono.





DZINA________________ Nambala yanu________

Adiresi yanu________________

## MAYESO A PHUNZIRO 7

Kubvomereza:

Ndaphunzira kuloweza mawu apamtima Marko 4:41 ndipo ndawabwereza kuuza mnzanga. (Lembani dzina lanu.)________

Ndawerenga ndime zonse zimene zinalembedwa pa phunziro 7. (Lembani dzina lanu.)________

___1. **Pamene Yesu anakhalitsa bata mphepo ndi nyaja anali kusonyeza kuti (1) Iye sanali kukonda madzi, (2) bwato anakwerayo anali wochepa, (3) Iye anali ndi mphamvu pa chilengedwe.**

___2. **Yesu atatontholetsa nyanja ija Iye anayamba kudzudzula ophunzira (1) pokhala opanda chikhulupiriro, (2) posapalasa bwato kupita mwamsanga kumtunda, (3) poyenda pamodzi naye.**

___3. **Pamene Yesu anachiritsa munthu wogwidwa ndi mzimu wonyansa Iye anali kusonyeza kuti (1) Iye analibe chifundo ndi munthuyo, (2) Iye anali kuchita mantha ndi mzimuyo, (3) Iye anali ndi mphamvu koposa chimzimu chonyansacho.**

___4. **Pamene munthu amene anali ndi mzimu wonyansa anachiritsidwa ndipo anafuna kutsatira Yesu; Yesu anamuuza kuti (1) zoonadi lowa m'bwato, (2) anaiwala kuti anakumana naye, (3) muka ndi kukauza anthu amtundu wake zimene Ambuye amuchitira Iye.**

___5. **Mzimayi wina anakhuza zobvala za Yesu chifukwa (1) mayiyo anafuna kungogwira ndi kudziwa mtundu wa nsaru, (2) mayiyo anali ndi chikhulupiriro ndi mphamvu zake za Yesu kuti zimuchiritsa, (3) munthu wina anamukankha mayi uja kotero kuti anakakhudza Yesu.**

___6. **Yesu anafuna kumudziwa mkazi amene anachiritsidwa pongokhudza chobvala chake kufuna kuti (1) amudalitse ndikumulimbikitsa, (2) amudzudzule ndi kumukalipira, (3) amulipiritse ndalama.**

___7. **Yairo anafunafuna chithandizo cha Yesu chifukwa (1) iye anali kudwala, (2) mwana wake wamkazi anali kudwala, (3) mkazi wake anali kudwala.**

___8. **Yesu asanafike kunyumba ya Yairo, panafika uthenga wonena kuti mwana wamkazi wa Yairo uja (1) wadwala kwambiri, (2) wachira tsopano, (3) wamwalira.**

___9. **Pofuna kuti alandire chithandizo chochokera kwa Yesu, Yairo anayenera kuiwala (1) kunyada kwake, (2) mwana wake wamkazi, (3) mkazi wake.**